**Uthenga wa Papa Francisco wa Lamulungu la Chibalalitso la 2024.**

20 October 2024

**Pitani, kaitaneni aliyense ku phwando (Mt. 22.9)**

Okondeka abale ndi alongo!

Mutu umene ndausankha kuti utsogolere chaka cha Chibalalitso cha Mpingo cha chaka chino watengedwa m'fanizo lochokera mu Uthenga Wabwino la phwando la ukwati *(Mt. 22:1-14)*. Anthu oitanidwa aja atakana kupita kuphwandolo, mfumu ija, yomwe inali mwini phwando ikuuza antchito ake kuti: 'Pitani tsono ku mphambano za misewu, mukaitane aliyense amene mukampeze' *(V. 9)*. Posinkhasinkha za mfundo yaikulu m'mawuwa molingana ndi fanizoli ndinso moyo wa Ambuye Yesu omwe, titha kupezamo zinthu zingapo zofunikira zotithandiza pofalitsa Uthenga Wabwino. Izitu zikubwera panthawi yake kwa ife tonse ophunzira a Khristu pamene tikufika kumapeto kwa Sinodi yomwe mawu ake oitsogolera akuti 'Chiyanjano, Kutenga nawo mbali, utumiki poikanso chidwi chake pantchito yake yoyamba yomwe ndi kulalika Uthenga Wabwino pa dziko lonse lapansi leroli.

1. ***'Pitani ndipo mukawaitane!' Kufalitsa Uthenga Wabwino ndi ntchito yosalekeza yopita kukaitanira ena Phwando la Ambuye.***

M'mawu a mfumu, mwini phwando ija kwa antchito ake, tikupezamo mawu awiri amene amafookoz chithimethime cha utumiki mu mawu oti 'Kupita' ndi 'Kuitana'.

Pa mawu oyambawo, tiyenera kukumbukira kuti antchitowo adali atatumidwa kale ndi mfumu ija kuti akaitane anthu oitanidwa ku phwando *(V3-4)*. Tikuona kuti kufalitsa uthenga wabwino ndi ntchito yosalekeza yoyendera anthu ndi kuwaitana kuti akumane ndi kukhala abwenzi a Mulungu. Mulungu yemwe ndi wachikondi chozama komanso chifundo chopanda malire nthawi zonse amafunitsitsa kukumana ndi anthu ake ndi kuwaitanira ku Chikondwerero cha ufumu wake ngakhale anthuwo asaonetse chidwi chenicheni kapena kukana kumene. Yesu Khristu m'busa wabwino ndinso Wamthenga wa Mulungu Atate adabwera kudzafunafuna nkhosa zosochera pakati pa aIsraeli ndipo adafunitsitsa kuti akasakenso ngakhale nkhosa zomwe sizinali pakati pa a Israeli *(Yoh. 10:16)*. Ali pansi pano, ngakhalenso atauka kwa akufa, Yesu adauza ophunzira ake kuti 'Pitani tsono!' komwe kunali kuwaitanira ophunzirawo ku ntchito yake yomwe, yofalitsa Uthenga Wabwino *(Lk. 10:3, Mk. 16:15)*. Kumbali yake komanso pokhulupirika ku ntchito yofalitsa Uthenga Wabwinoyi yomwe adalandira kuchokera kwa Ambuye Yesu, Mpingo upitiriza kupita mpaka kumalekezero a dziko lapansi kukalalika mosatopa kapena kutaya mtima ngakhale ukumane ndi zovuta zowulepheretsa ntchitoyi.

Ndikukufuna nditengerepo mwayi wothokoza Amishoni onse amene atamva kuitana kwa Yesu Khristu adasiya zonse ndi kupita kumadera akutali kuti akalalike Uthenga Wabwino kumalo kumene anthu sadamvebe Uthengawu kapena angoumva kumene. Abale ndi alongo okondeka, kudzipereka kwanuku kukuulula kotheratu chidwi chomwe muli nacho chofuna kukwaniritsa udindo womwe Yesu adasiira ophunzira ake woti: 'Pitani kwa anthu a mitundu yonse, mukawasandutse ophunzira anga' *(Mt. 28:9).*Tipitirize kupemphera ndi kuthokoza Mulungu chifukwa cha Amishoni atsopano ndi ochuluka amene akuvomera kuitanidwa kwawo kuti akhale alaliki a Uthenga Wabwino mpaka kumalekezero a dziko lapansi.

Tisaiwale kuti Mkhristu aliyense ndi woitanidwa kuti atenge nawo gawo pa utumiki umenewu; pochitira umboni Uthenga Wabwinowo mwa njira iliyonse kuti choncho Eklezia yense athe kupita mosabwerera m'mbuyo 'kumphambano' zosiyanasiyana za padziko lapansi lero lino. 'Chodabwitsa kwambiri mu mpingomu lero lino n'choti, Yesu amagogoda pakhomo pathu ali m'kati momwemo kuti timulole atulukemo! Kawirikawiri timakhala mpingo womwe sukufuna kuti Yesuyo atuluke panja, mpingo umene umangofuna kuti Yesu Khristu akhale wake yekha' pomwe Khristu mwini wakeyo adabwera kudzafalitsa Uthenga Wabwino ndipo akufunanso kuti ife tikhale Amishoni *(Zomwe zidanenedwa kwa nthumwi pamsonkhano wokonzedwa ndi nthambi yoyang'anira Akhristu eni ake ndi mabanja pa 18 February, 2023*). Tiyeni akhristu tonsefe

tikhale okonzeka, aliyense malinga ndi maitanidwe ake, kuyambitsa ntchito yatsopano yofalitsa Uthenga Wabwino, monga mmene zidalili pamene Chikhristu chimayamba paja.

Tikayang'ananso mawu omwe mfumu yokonza phwando ija idapereka kwa antchito ake m'fanizo lija, antchitowo sakungowuzidwa kuti 'apite' koma kuti 'akaitanenso anthu.' 'Bwerani ku phwando la ukwati' *(Mt. 22:4).* Apatu tikuonanso chinthu china chofunikira pantchito yautumiki womwe Mulungu adatipatsa. Titha kunena kuti antchitowa adakapereka uthenga wa mbuye wawoyu mwachangu zedi komanso mwaulemu ndi mwachikondi. Ntchito ya utumiki yofalitsa uthenga wabwino kwa munthu aliyense iyeneranso kutsanzira momwe yemwe tikumulalikayo akadalalikira. Polalika ku dziko lapansi za 'kukoma kwa chikondi chopatsa moyo cha Mulungu chomwe chidaoneka mwa Mwana wake Yesu Khristu amene adafa ndi kuuka kwa akufa *(Evangelii Gaudium, 36*), alaliki ake alalike ndi chimwemwe, mphamvu komanso chikondi zomwe ndi zipatso za Mzimu Woyera yemwe akugwira ntchito mwa iwo *(Gal. 5:22)* osati powakakamiza kapena kuwanyengerera koma pokhala nawo pafupi, kuwaonetsa chifundo ndi chikondi kenaka ndi kumasinkhasinkha nawo limodzi za Mulungu ndi momwe amachitira zinthu zake.

### 2. *'Kuphwando la ukwati.' Phwando lakumwamba ndi phwando la Ukaristia zigawo za utumiki wa Khristu ndi Mpingo.*

M'fanizoli, mfumu ikuuza antchito ake kuti akapereke uthenga woitana anthu kuphwando la ukwati wa mwana wake. Phwando limeneli, likufanizira phwando la kumwamba. Phwandoli ndi chithunzithunzi cha chipulumutso chenicheni cha anthu mu Ufumu wa Mulungu chomwe chapherezera kale mu kubwera kwa Yesu, Mpulumutsi wathu ndinso mwana wa Mulungu amene adatipatsa moyo, moyo wake ochuluka *(Yoh 10:10)*, wofaniziridwa ndi tebulo la chakudya chokoma ndi vinyo wabwino, pomwe Mulungu adzaonongeretu imfa mpaka kalekale *(Yesaya. 25:6-8).*

Ntchito ya Yesu Khristu ndi yofuna kufikitsa zinthu pachimake penipeni monga momwe iye mwini adanenera pomwe amayamba kulalika pansi pano kuti 'Nthawi yakwana, ufumu wa Mulungu wayandikira' *(Mk. 1:15)*. Ophunzira a Yesu Khristu akuitanidwa kuti apitirize ntchito ya Mbuye wawo yolalika Uthenga Wabwino. Apatu tikusinkhasinkha za zomwe Aepiskopi adatiphunzitsa ku msonkhano wawo wachiwiri wa ku Vatican zoti ntchito ya Mpingo yofalitsa Uthenga Wabwino ili ndi maonekedwe a phwando la kumwamba pomwe adati: 'Nthawi yolalika Uthenga Wabwino ili pakati pa nthawi yomwe Ambuye adabwera koyamba ndi pomwe adzabwerenso kachiwiri … potitu Uthenga Wabwino uyenera kulalikidwa ku mayiko onse Ambuye Yesu asadabwerenso *(Mk. 13:10' (Ad Gentes, 9).*

Tikudziwa kuti pakati pa Akhristu oyamba aja chidwi chawo pa utumiki chinali cha uthenga wamphamvu wa kubweranso kwa Yesu Khristu ndinso phwando lakumwamba. Iwowa adaona kufunika kolalika Uthenga Wabwino mwachangu. Leronso, n'kofunika kuchita chimodzimodzi chifukwa zitithandiza kulalikira ndi chimwemwe cha iwo amene akudziwa kuti 'Ambuye ali pafupi kubwera' komanso ndi chikhulupiriro cha amene akuyang'ana kutsogolo pomwe tonse tidzakhale ndi Yesu Khristu pa phwando lake la ukwati mu ufumu wa Mulungu. Pamene dziko lapansi likutipatsa 'maphwando' osiyanasiyana amene ambiri a iwo ndi ongoonetsa mtima wofuna kukhala ndi zinthu zambiri, kudzikonda, kukondetsa chuma ndinso mtima wongodziganizira tokha basi, Uthenga Wabwino ukutiitanira tonse ku Phwando la kumwamba lomwe ndi lobweretsa chimwemwe, kugawana, chilungamo ndi umodzi poyanjana ndi Mulungu ndi anthu amnzathu.

Moyo wathunthuwu, womwe ndi mphatso ya Khristu, timauyembekezeradwabe ngakhale tsopano mu phwando la Ukaristia lomwe mpingo umachita potsatira lamulo la Ambuye kuti tiziwakumbukira. Kuitanira anthu onse ku phwando la kumwamba ndi kolumikizana kwambiri ndi kuitanira aliyense ku guwa la Nsembe ya Ukaristia pomwe Ambuye Yesu amatidyetsa tonse ndi mawu awo komanso ndi thupi ndi magazi awo. Monga mmene Papa Benedicto XVI adatiphunzitsira, 'Nsembe iliyonse ya misa imafanizira kusonkhana kwa anthu a Mulungu kumwamba. Kwa ife, phwando la Ukaristia limatilawitsiratu phwando lotsiriza lomwe aneneri analosera kale *(Yesaya. 25:6-9)* lomwenso chipangano chatsopano limalitchula kuti 'Phwando la Ukwati la mwana wa nkhosa *(Chiv. 19:9)* lomwe lidzakondwereredwe ndi chimwemwe m'chiyanjano cha Oyera' *(Sacramentum Caritatis, 31)*

Nchifukwa chake tsono, tonsefe tikuitanidwa kulandira Ukaristia kawirikawiri m'zigawo zake zonse koma makamaka m'zigawo zomwe zimatikumbutsa za phwando lakumwamba ndinso la utumiki. Pachifukwachi, ndikufuna kubwereza kunena kuti 'Sitingathe kufika paguwa la Nsembe ya Ukaristia popanda kutumidwa kukhala alaliki a Uthenga Wabwino, womwe umafumira mu mtima mwa Mulungu kuti ukafikire anthu onse' *(Sacramentum Caritatis, 31).* Kusinkhasinkha za Ukaristia mwa njira zatsopano pambuyo pamliri wa Covid – 19, kukhala kofunika zedi pofuna kwambiri pofuna kubwezeretsa chidwi cha moyo wa utumiki mwa mkhristu aliyense. Kodi tikhale ndi chikhulupiriro chochuluka bwanji kapenanso chidwi chotani chochokera m'mitima mwathu kuti tizinena pa misa iliyonse kuti: 'Tili kulalika imfa yanu Ambuye, ndi kuvomereza kuuka kwanu mpaka mudzabwererenso!'

Chaka chino chomwe tachiikiza m'mapemphero pokonzekera jubili ya 2025, ndikufuna ndikulimbikitseni nonse kuti muzamitse kudzipereka kwanu komanso kutenga nawo mbali pa Nsembe ya Ukaristia komanso kupempherera ntchito wa mpingo wofalitsa Uthenga Wabwino. Potsatira lamulo la Mpulumutsi wathu, Eklezia saleka kupemphera pa Nsembe ya misa iliyonse ndi miyambo ina ya mapemphero pemphero la 'Atate athu' ndi pempho lake loti 'Ufumu wanu udze!' Potero, pemphero la tsiku lililonse komanso makamaka Nsembe ya Ukaristia zimatithandiza ife kukhala ndi anthu amene tili pa ulendo ndinso atumiki a chiyembekezo, amene tikupita ku moyo wosatha mwa Mulungu, kulowera ku phwando la ukwati lomwe Mulungu adakonzera ana ake onse.

### 3. *'Aliyense.' Utumiki wa pa dziko lonse lapansi wa ophunzira a Khristu mu mpingo ochitira zinthu limodzi ndi otumikira.*

Mfundo yachitatu ndinso yotsiriza yomwe tikuisinkhasinkha ndi yokhudza anthu omwe adalandira uthenga wa mfumu wowaitana ku phwando woti 'Aliyense.' Monga ndinatsindika kale, 'Ichi ndi chithimethime cha utumiki: kuti 'aliyense' osasiyako wina, ayitanidwe. Utumiki wathu uliwonse umafumira mu mtima mwa Khristu kuti aitanire anthu onse kwa iye' *(Zomwe zidanenedwa pamsonkhano waukulu wa Mabungwe a Utumiki wa Apapa pa 3 June 2023)*. Lero, m'dziko lapansi momwe muli kugawikana ndi mikangano, Uthenga Wabwino wa Khristu ukupitiriza kukhala liwu lofatsa koma lamphamvu loyitana munthu aliyense kuti akumane ndi mnzake ndi kuzindikira kuti iwo ndi abale ndi kusangalala mu umodzi wawo ngakhale ali anthu osiyana. 'Mulungu mpulumutsi wathu amafuna kuti anthu onse apulumuke ndipo kuti adziwe choona' *(1 Timoteo 2:4)*. Tisaiwale tsono kuti pa Utumiki wathu tikukupemohedwa kulalika uthengawo kwa aliyense: 'Mmalo mooneka ngati tikufuna tikuwakakamiza ndi malamulo atsopano, tiyeni tikhale anthu amene tikufuna kugawana nawo chimwemwe chawo, amene tikuwalozera moyo wabwino ndinso amene tikuwaitanira phwando la zakudya zokoma' *(Evangelii Gaudium, 14).*

Atumiki a Khristu nthawi zonse amakhala ndi chidwi chenicheni ndi anthu onse posatengera ulemu womwe ali nawo m'dziko kapena makhalidwe awo. Fanizo la phwando la ukwatili likutiuza kuti potsatira lamulo la mfumu, antchito aja adakaitana 'aliyense amene adamupeza posatengera kuti anali wabwino kapena woipa' *(Mt. 22:10)*. Ambiri a oitanidwawo anali 'osauka, otsimphina, akhungu ndi aulumali' *(Lk. 14:21)*, kapena mwachidule anthu onyozeka kwambiri mwa onse, anthu amene dziko limawataya, ndiwo alendo apaderadera a mfumu. Kuphwando la ukwati la mwana wake lomwe Mulungu adakonza, aliyense ali woitanidwa chifukwa chikondi chake pa aliyense mwa ife ndi chozama komanso chopanda malire. 'Mulungutu adawakonda kwambiri anthu a padziko lapansi anali naye mwana mmodzi yekha komabe adampereka mwana wake mmodzi yekha kuti aliyense wokhulupirira mwanayo asatayike koma akhale moyo wosatha' *(Yoh 3:16).* Munthu aliyense, bambo kapena mayi akuitanidwa ndi Mulungu kuti agawane naye chifundo chake chomwe chimatisintha ndi kutipulumutsa. Munthuyo akungoyenera kuvomera mphatso yaulere ndi yoyerayi, kuivomera ndi kuilola kuti imusinthe, poivala ngati 'chovala cha ukwati' *(Mt. 22:12).*

Kuti tithe kufalitsa Uthenga Wabwino kwa onse, Utumiki wa aliyese ukusoweka kudzipereka kwa aliyense ku ntchitoyi. Tikuyenera kupitiriza ulendo wathu mu Mpingo ochitira zinthu limodzi ndi otumikira pa ntchito yofalitsa Uthenga Wabwino. Mpingo ochitira zinthu limodzi ndi mpingo otumikira, chimodzimodzinso kutumikira ndi kuchitira zinthu limodzi. N'zachidziwikire tsono kuti kugwirana manja potumikira n'kofunika

zedi masiku ano, mu Mpingo wonse ndinso m'matchalitchi athu onse mu Mpingowu. Potsanzira maphunzitso a Aepiskopi ku Msonkhano wachiwiri wa ku Vatican ndinso zomwe Apapa ena onse omwe ndidalowa m'malo mwawo, ndikupereka ku ma Dayosezi onse pa dziko lonse lapansi ntchito za Mabungwe autumiki wa Apapa. Ntchitozi zimapereka zida zoyambirira 'zomwe Akatolika ali nazo kuyambira pachiyambi zokhala ndi mtima wa umishoni ndiponso ndi njira zopezera ndalama zomwe Amishoniwa angagwiritsire ntchito, aliyense malinga ndi zosowa zake' *(Ad Gentes, 38)*. Pachifukwa ichi, chopereka chonse cha Lamulungu la Chibalalitso m'matchalitchi onse chiyenera kupita ku thumba la Mpingo wonse kuti nthambi ya Utumiki wa Apapa yofalitsa Chikhulupiriro chathu m'malo mwa Apapa azigawe ndalamazo potengera zosowa za mautumiki a mpingo ofalitsa Uthenga Wabwino padziko lonse. Tiyeni tipemphere kuti Mulungu kuti atitsogolere ndi kutithandiza kukhala Mpingo ochitira zinthu limodzi ndi otumikira *(Ulaliki wa pa misa yotsekera msonkhano waukulu wa Aepiskopi wa Sinodi ya Aepiskopi, 29 October, 2023).*

Pomaliza, tiyeni tikweze maso athu kwa Amayi Maria, amene adapempha Yesu mwana wawo kuti achite mlakuli wake woyamba pa ukwati wa ku Cana ku Galileya *(Yoh 2:1-12).* Ambuye Yesu adapereka kwa akwatiwo ndinso anthu onse oitanidwa ku ukwatiwo mphatso ya vinyo watsopano ndinso wochuluka ngati chinthu cholosera phwando la ukwati lomwe Mulungu akukonzera anthu onse kumapeto a moyo uno. Tipemphe uneneri wa Amayi Maria amayi athu pa ntchito ya utimiki ophunzira a mwana wawo yofalitsa Uthenga Wabwino lero. Ndi chimwemwe komanso chikondi cha amayi athu, ndi mphamvu zawo zofumira mu kukoma mtima ndi chikondi kwawo *(Evangelii Gaudium, 288)* tiyeni tinyamuke tikaitane aliyense kuphwando la Mfumu, Mpulumutsi wathu. Maria Woyera, Nthanda ya amene akufalitsa Uthenga Wabwino, mutipempherere ife!

Yaperekedwa ku tchalitchi la Yohane Oyera. Lateran Basiilica pa 25 January, 2024, pa Chaka cha Kutembenuka mtima kwa Paulo Woyera.

Papa Francisco.